Mzimu Woyera Unathandiza Samisoni Kukhala ndi Mphamvu

OWERUZA CHAPUTALA 13 MPAKA 16



www.jw.org/ny © 2015 Watch Tower Bible and Tract Society of Pennsylvania

WERENGANI OWERUZA 16:3.

AFILISITI **ANKAKWIYA** KWAMBIRI SAMISONI AKAWAGONJETSA. CHONCHO ANASONKHANA KUTI AKAMBIRANE MMENE **ANGAMUGONJETSERE.**

SAMISONI **SITINGAMUGONJETSE**

TADIKIRANI... NDIKUDZIWA **ZIMENE TINGACHITE**...

AFILISITI ANAKONZA ZOTI MKAZI YEMWE SAMISONI ANKAMUKONDA KWAMBIRI, DZINA LAKE **DELILA, APUSITSE** SAMISONIYO N'CHOLINGA CHOTI **ANENE KUMENE KUMACHOKERA MPHAMVU ZAKE.**

KODI IWE SAMISONI **MPHAMVU** ZAKO ZIMACHOKERA KUTI?

USANDIBISIRE. **TANDIUZE,** MPHAMVU ZAKO ZIMACHOKERA KUTI?

NGATI **UMANDIKONDADI,** SUNGANDIBISIRE.

CHABWINO, NDI... **TSITSI LANGA.**

SINDINAMETEPO TSITSI LANGA.

www.jw.org/ny © 2015 Watch Tower Bible and Tract Society of Pennsylvania

DELILA ANAKONZA ZOTI AFILISITI **AGONJETSE** SAMISONI.

SAMISONI ATAGONA, MUNTHU WINA **ANAMETA TSITSI LAKE LONSE.** KENAKO AFILISITI **ANAMUBOOLA MASO** N'KUPITA NAYE KU **GAZA.**

SAMISONI ALI M'NDENDE, **ANADANDAULA KWAMBIRI** NDI ZIMENE ANACHITAZO.

SINDINACHITE BWINO **KUMUUZA** KUMENE MPHAMVU ZANGA ZINKACHOKERA.

CHONDE YEHOVA **NDIKHULULUKIRENI.** PEPANI KWAMBIRI.

AFILISITI ANACHITA **PHWANDO** LALIKULU KUTI **ALEMEKEZE MULUNGU WAWO** DZINA LAKE DAGONI NDIPO ANATULUTSA SAMISONI KUTI **AZIMUSEKA.**

IWE, SAMISONI, NDANI ALI NDI MPHAMVU **TSOPANO?**

DAGONI NDI WAMPHAMVU KWAMBIRI KUPOSA **MULUNGU WA SAMISONI.**

www.jw.org/ny © 2015 Watch Tower Bible and Tract Society of Pennsylvania

AFILISITI **ANKANYOZA** KWAMBIRI SAMISONI NDIPONSO YEHOVA. KOMA **TSITSI** LA SAMISONI LINALI **LITAMERA**...

MULUNGU WAMPHAMVUYONSE YEHOVA, CHONDE **MUNGONDIPATSANSO MPHAMVU** KAMODZI KOKHA.

SAMISONI ANAGWIRA **ZIPILALA** ZA NYUMBAYO NDIPO **ANAZIKANKHA** KWAMBIRI.

YEHOVA ANAMUPATSA **MZIMU WOYERA** KUTI AKHALENSO **WAMPHAMVU** NGATI KALE.

SAMISONI **ANAWONONGA** AFILISITI AMBIRI OMWE ANAKHALA AKUZUNZA AISIRAELI KWA NTHAWI YAITALI.

KODI TIKUPHUNZIRAPO CHIYANI PA NKHANIYI?

KODI MPHAMVU ZA SAMISONI **ZINACHOKERA** KUTI?

LEMBA LOKUTHANDIZANI: OWERUZA 13:25.

KODI SAMISONI **ANAPEZANSO** BWANJI MPHAMVU?

LEMBA LOKUTHANDIZANI: OWERUZA 16:28.

KODI **INUYO** MUNGALANDIRE BWANJI MZIMU WOYERA WA MULUNGU?

LEMBA LOKUTHANDIZANI: LUKA 11:13.

www.jw.org/ny © 2015 Watch Tower Bible and Tract Society of Pennsylvania